NYA_TTB_0943_20161109_script

Danieli : 11:37-45

Mutu : Ufumu wodziika ndiwo wanthawiyochepa

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyeni titsogozedwe ndi mau a Mulungu amene akupezeka pa Ahebri 10:31, amene akuti, “Kugwa m’manja a Mulungu wamoyo nkoopsa.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula Danieli 11:15-36, pamene timakambirana za munthu wa uchimo. Ndipo lero pa Danieli 11:37-45, tiona za ufumu wodziika kuti ndiwo wanthawiyapang’ono.

37. Ndipo sidzasamalira milungu ya makolo ake, kapena choikhumba akazi, kapena kusamalira milungu iri yonse; pakuti idzadzikuza koposa onse.

Poyamba ndifuna tigwire mau akuti, “Ndipo siidzasamalira milunguya makolo ake, kapena choikhumba akazi, kapena kusamalira milungu iliyonse.”Mau awa akutanthauza kuti mfumu yomwe ndi yotsutsa Kristu, siidzasamalira milungu ya makolo ake.Kapena kunena kuti siidzamangiriridwa ku milungu ya makolo

ake, dziko lake kapenanso chipembedzo chake.Iyeyu adzapembedzamulungu wina aliyense amene afuna kapena kuti sadzapembedzamulungu wina aliyense wa makolo ake. Kutsimikiza kuti chinthu chimene chimamanga anthu kuchipembedzo cha makolo awo, sichidzagwira ntchito kapena kuti sichidzakhalachamphamvu.

Ndiye pamene tiwerenga mau onse apa Danieli 11:36, tipeza kuti ndiwo onse akukwaniritsa zinthu zonse zomwe tanenazi. Tamvani akuti, “Ndipo mfumu idzachita monga mwa chifuniro chake, nidzadzikweza, ndi kudzikuza koposa milungu iri yonse nidzanenazodabwitsa pa Mulungu wa milungu, nidzapindula, mpaka udzachitidwaukaliwo; pakuti chotsimikizikam’mtimacho chidzachitika.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndi mau amenewa ndifuna muone kuti mau onse anenedwawaakutsimikizira kuti mfumu yotsutsa Kristu ndiyo Antiokasi. Ndikunena mau amenewa chifukwa Antiokasi Epiphane, anali kulambira milungu yomwe anali kuikhumba, m’dziko lake, kapena mwina milungu yomwe a Greek kapenanso Aroma anali kulambira.

Komanso taonani kuti m'malo molemekezamulunguwa makolo ake, iye akutenga fano la Jupiter ndi kukaliika m'Kachisi wa a Yuda, mu Yerusalemu. Kutsimikiza kuti sanali kulabadira milungu ya makolo ake.Zinthu zonsezi zikuchitika chifukwa chakuti Antiokasi anaphunziram'maiko akunja, kotero kuti sanalemekezekotheratu milungu ya dziko lake.Tere, m'njira zambiri, tikuona kuti Antiokasi ndiye munthu amene analibe chikhulupiriro mwa milungu ya makolo ake.Komanso ndiye amene anaonetsa kudzikweza ndi kupanga malamulo ndi cholinga chofuna kuchotsa chipembedzo cha dziko lake, ndi kubweretsa milungu ya a Greek. Tikunena kuti ngakhale mafumu ena m'mbuyo mwake anali kulemekeza Mulungu wa Israyeli namapereka mphatso zawo m'Kachisi ku Yerusalemu, koma iye ananyazitsa Mulungu ameneyu kopambana.

Ndiye tikunenetsa kuti Antiokasi ndiye amene akuimira wotsutsa Kristu, monga Kristu ali Mulungu wa wokhulupirira, uyu ndiye wotsutsa Kristu amene amati ndiye wochokera kumuzuwomwewo,koma sapembedza Kristu ngakhale pamene anena kuti ndiye wansembe.

Kachiwiri, tikuona kuti kusalabadira zokhumba za akazi zikungotsimikizadi mtima woipitsitsawa Antiokasi, umene sumakhudzidwa ndi chinthu chilichonse chimene anthu ena aulemu wawo amachilemekeza. Ndiye tikunena kuti kusalemekeza milungu ya dziko lake, yomwe ndiyongosangalatsa thupi, zikutsimikizadi kuipa kwenikweni kwa Antiokasi.

Tsono poumbamkotamau akusalabadira zokhumba za akazi a chiHebri, amene amalakalaka atakhala mayi wake wa Mesiya, zikutsimikizadi kuti Ambuye Yesu Kristu, adzakanidwa kukhala m'dani wake. Kutsindika mau akuti wotsutsa Kristu ndiye amatsogolerakuukira Mulungu ndi Kristu. Monga mwa mau aja ali pa Masalmo 2:2-3, amene akuti, "Adzakhazikitsa mafumu a dziko lapansi, nachitaupo akulu pamodzi, kutsutsana naye Yehova, ndi wodzozedwa wake, ndi kuti tidulezomangira zawo, titayensinga zawo."

Wokondedwa anzanga apaulendo, wotsutsa Kristu uyu, ndiye amene adzatsutsazipembedzo zonse za padziko lapansi, ndi cholinga chakuti munthu aliyense amlambire iye. Tikunena kuti wotsutsayu si ndiye wopembedza kokha, koma

wolimbikitsakupembedza kumene, popeza iye ali momwemo. Pachifukwa chimenechi, tikuona kuopsakwa masiku otsiriza popeza wotsutsayu adzagwiritsa ntchito mau akuti, “Chipembedzo chimodzi, m’dziko limodzi.” Kutanthauza kuti ichi, chidzakhala chiyambi cha chibvuto chachikulu (The Great Tribulation), chidzachokera pa mau a chipembedzo chimodzi, kotero kuti wina aliyense amene adzakane chipembedzo chimenechi, ndiye adzalowa mu bvuto limeneli. Ichi, ndichimene akunena Yohane pa Chibvumbulutso 13:15-17, pamene akuti, “Ndipo anachipatsa mphamvu yakupatsa fano la chirombompweya, kutinso fano la chirombolilankhule, nilichite kuti onse osalilambira fano la chiromboaphedwe. Ndipo chochita kuti onse, ang’ono ndi akuru, achuma ndi osauka ndi mfulu ndi akapolo, alandira chilembo pa dzanja lawo ndi pamphumi pawo; ndi kuti munthu sangakhozekugula kapena kugulitsa, koma iye yekha wakukhala nacho chilembo, ndilo dzina la chirombo kapena chiwerengelo cha dzina lake.” Mau onsewa akutsimikiza kuti m’nthawi ya chibvuto chachikulu munthu aliyense amene sadzakhala ndi chizindikiro cha chilembo cha chipembedzo cha 666, ndiye amene adzalowam’chibvuto chimenechi, popeza sadzakhoza kugula ndi

kugulitsapamsika uliwonse.Ndipo sikudzatheka ngakhale kukwera bus popanda chilembo chimenechi.Kodi inu mwakonzekera kulowa m'chibvuto chimenechi?

38. Koma kumalo kwake idzachitira ulemu Mulungu wa malinga; ndi mulungu amene makolo ake sanaudziwa, adzaulemekeza ndi golidi, ndi siliva, ndi miyala ya mtengo wake ndi zinthu zofunika.
39. Ndipo adzachita molimbana ndi malinga olimba koposa, pomthandiza Mulungu wachilendo; ali yense wombvomerezaadzamchurukitsira ulemu, nadzawachititsa ufumu pa ambiri, nadzagawa dziko mwa mtengo wake.

Tsono pamene tilondola mau akuti, "Idzachitira ulemu Mulungu wa malinga," akutanthauza kuti mfumu iyi, idzalemekezamulunguwa malinga m'malo mwa mulungu wa makolo ake. Kunena kuti mfumu iyi, siidzalabadiramulungu aliyense koma kulambira mulungu wake yekhayo. Uyu, ndiye mulungu amene alipa ufumu, umene uli pamalo omwewo osasintha konse. Kutsimikiza kuti Antiokasi anali kutenga komanso kulemekeza ufumu kopambana kuposa china chilichonse.Antiokasi anali munthu

wodabwitsapopeza sanali kulabadira milungu ya makolo ake, ndipo sanali kumangiririkakumalamulo a chipembedzo chawo.Ndipo sanali kusamala maganizo ena aliwonse a munthu, popeza amatenga kuti ndizo nzeru zofooka za mkazi, kotero kuti anali kungodalira pa mphamvu za ufumu wake.Kutsimikiza kuti Antiokasi anangoikamaso ake, pa ufumu wake basi, osati pa chinthu china chilichonse ayi. Tere, ndichifukwa chake iye anasankha Jupiter kukhala mulunguwa nkhondo, mulungu wa Aroma, fano lomwe likuimira ufumu wamphamvu wa a Roma, padziko lonse lapansi.Ndiye mphamvu za ufumuwu kapena mulungu ameneyu zagona pa ndalama. Mwanjira ina tikunena kuti Antiokasi anaika mtima wake kwambiri pa ndalama zomwe amaona kuti ndiyo mphamvu yake. Momwemonso lero lino ndalama ndilo fano lalikuru padziko lonse lapansi kwa anthu ambiri, chifukwa cha ganizo lomwelo lakuti zimapereka mayankho kwa zinthu zonse. Kodi ganizo ilindiloona kwa inu?

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano ndifuna kutsimikiza kuti ino, ndiyo nthawi ya satana.Taonani akuchita china chilichonsechothekakuzunza ndikugonjetsa wokhulupirira,

popezaakudziwakuti nthawi yake yatha. Pachifukwa chimenechi, ndifuna kuti inu ndi ine, tilimbikitsidwe ndi mau apa Chibvumbulutso 12:12, amene akuti, “Chifukwa chake kondweranimiyamba inu, ndi inu akukhala momwemo. Tsoka mtunda ndi Nyanja, chifukwa mdierekezi watsikira kwa inu, wokhala nawo udani waukuru, podziwa kuti kamtsalira kanthawi.”Ndiye tikunenetsa kuti wotsutsa Kristu ndichipangizo chimodzi chofewa, chimene chikhozakumvera ganizo lina lililonse limenechidzatumikiranalo satana kotheratu, m’masiku amenewo.Iyeyu adzalamulira mitima ya ambiri nadzachita ndi zinthu zake monga afuna.Iyeyu, ndiye mfumu yodziika yokha pampando, amene ndiye wolamulira wankhaza wotsiriza padziko lonse lapansi.

40. Ndipo nthawi yotsiriza mfumu ya kumwela idzalimbana naye, ndi mfumu ya kumpoto idzamdzera ngati kabvumvulu, ndi magareta, ndi apakavalo ndi zombo zambiri; nadzalowam’maiko, nadzasefukira ndi kupitirira.

Poyamba tiyeni tigwire mau akuti, “ndipo nthawi yotsiriza.”Iyi, ndiyo nthawi yomwe iyenerakudziwika kuti ndiyo nthawi yomwe

ndipothera pa zinthu zonse zimene zinachitika m'mbuyomo.Mwanjira ina "nthawi yotsiriza" iyi, ndiyo yokwangula kapena kuti nthawi ya zomwe zidzachitika pakutha kwa zinthu zonse zimene mngelo adanena pa Danieli 10:21, kuchokera mnthawi ya ulamuliro wa Dariyo, m'Medi mpaka Danieli 11:1, kufikira kumapeto kwa ulamuliro wa Antiokasi.Iyi, ndi nthawi yomwe ndi yotalikakokwanira zaka 350.Ndipo mwa zaka zimenezi, Antiokasi analamulira zaka khumi ndi chimodzi chokha, kotero kuti ndiyo nthawi yomwe ikutchulidwa kuti ndiye nthawi yotsiriza. Koma tiyenera kudziwa kuti iyi, ndiyo nthawi yomwe ndiyowawitsazedikwa anthu a chiYuda, ngakhale kuti ndiyo nthawi yomwe inali yotsiriza, pamene mngelo anaikapo maso ake.

Tsono nkhani ikuti m'nthawi imeneyi, ndipo pamene mfumu ya kumweraidzaputa Antiokasi ndi cholinga chofuna kutenganso ulamuliro wamadera a Sidoni ndi Palestine, amene anali m'manja mwa Syria. Apa, ndipo pamene mfumu ya Syria, Antiokasi idzabwera ndi mphamvu zonse monga kambvulubvulu ndi kutenga dera la Memphis la ufumu wa Aigupto pamodzi ndi dziko la Israyeli.

Ndiye nkhani yonseyi ikulozera nthawi yotsiriza ya zinthu zonse, yomwe inakhazikitsidwa ndi Mulungu, pamene wotsutsa Kristu adzakhala pamwamba zedi, kapena kuti adzadzikweza kwambiri, chifukwa cha mphamvu ndi ulamuliro wake. Koma potsiriza pazonsezi, Mulungu adzabwera ndi mphamvu ndi kumwetula mtundu wa anthu a kumpoto, wa Russia.

41. Adzalowanso m'dziko lokometsetsalo ndi maiko ambiri adzapasuka; koma opulumuka dzanja lake ndi awa: Edomu, ndi Moabu ndi oyambaa ana a Amoni.

Nkhani ili mundime ino, ikunena kuti pamene Antiokasi adzalowanso m'dziko la Palestine, ndilo dziko lokometsetsalo, sadzaononga mitundu ina ya anthu monga a Edomu, Moabu ndi Ammon, amene ndi adani Israyeliakale lomwe. Kotero kuti mitundu inayi, ndi yomwe idzagwiritsidwa ntchito kuthandizirakuthyola Israyeli. Kunena kuti Antiokasi sadathekuthyola ma Arabu chifukwa ndiwo abale awo a Edomu, Moabu ndi Ammon. Mwanjira ina tikunena kuti maso ya Antiokasi ali pa Israyeli basi. Momwemonso wotsutsa Kristu akuika maso ake pa wokhulupirira onse, koma osati akunja ayi.Kutanthauza

kuti maso ya wotsutsa Kristu aikidwa pa kuzuza wokhulupirira, ndipo adzathandizidwa ndi anthu wosakhulupirira.

42. Adzatambalitsiranso dzanja lake kumaiko; dziko la Aigupto lomwe silidzapulumuka.

Tiyeni pano tigwire mau akuti “Adzatambalitsiranso dzanja lake ku maiko.” Mau awa akutanthauza kuti, wotsutsa Kristu adzayesetsa kumenya nkhondo ndi kutenga ulamuliro ngakhalenso pa maiko ena a ufumu wakumwera ndi wa kumpoto. Nkhani ikunena kuti mtundu wa a Edomu, Moabu ndi a Ammon adzathakuthawa nkhondo imeneyi, koma Aigupto ayi. Umu ndi muja tinaonera kuti dera la Memphis, linatengedwakale ndi kukhala muulamuliro wawotsutsa Kristu.

43. Ndipo adzachita mwamphamvu ndi chuma cha golidi, ndi siliva ndi zinthu zofunika zonse za Aigupto; Alubi ndi Akusiadzatsata mapazi ake.

Nkhani iyi, ikuchokera pa Danieli 11:28, pamene akukamba za mfumu Antiokasi atagonjetsa mfumu ya Aigupto ndipo atalandamadera ofunika kwambiri monga Memphis, ndipo

anabwerera kwawo ndi chuma ndi zinthu zina zofunika kwambiri zomwe zinakhala zake. Komanso mfumuyiinatenganso ulamuliro pamaderaaAlubi ndi kusi, amene ndimadera okhala pafupi ndi Aigupto. Mwanjira ina tikunena kuti popeza Aigupto anali paulamuliro wa Antiokasi, momwemonso madera a Alubi (Libya) ndi Kusi (Ethiopia), naonso anatengedwa ndi iye nakhala omvera ulamuliro wake. Ichi, ndichimene chikutsimikiza mau apa Ezekieli 30:5, amene akuti, “Kusi ndi Puti ndi Ludi ndi osokonezeka onse ndi Kubi ndi anthu a dziko lapangana nawo adzagwa pamodzi nawo ndi lupanga.” Izi, zikutanthauza kuti Alubi ndi Kusianatengedwa ukapolo chifukwa cha ubwezi wawo ndi Aigupto amene wakanthidwa ndi Antiokasi.Kutsimikiza mau akuti, kaluluanaferakumodzi ndi chitsamba.

Wokondedwa anzanga apaulendo, monga tinanena kale kuti Antiokasi ndiye amene akuimira wotsutsa Kristu, kotero kuti ndiye amene adzakhala ndi ulamuliro wa chuma chonse cha dziko lapansi. Kutanthauza kuti ndiye amene adzakhala ndi ulamuliro pa misika yonse ya dziko lapansi panthawi imeneyo.

44. Koma mbiri yochokera kum’mawa ndi kumpoto idzambvuta; nadzaturuka iye ndi ukari waukuru kupha ndi kuononga konse ambiri.

Ndime ino, ikuonetsa kugwa kwa mfumu yamphamvu, Antiokasi, amene anafika pamwamba kwambiri pa ulamuliro wake. Taonani iyeyu anadzazidwa komanso kudzikweza ndi kudzitama chifukwa cha nkhondo zomwe wakhala akugonjetsandi chifukwa cha chuma chomwe wakhala akukundika. Tsono iyi, ndiyo nkhani ija inalembedwanso pa Danieli 8:25, imene ikuti, “Ndipo kuchenjera kwake adzapindulitsa chinyengo m’dzanja mwake, nadzadzikuza m’mtima mwake, ndipo posatekeseka anthu, adzaononga ambiri; adzaukiransokalongawa akalonga, koma adzathyoledwa popanda dzanja.”

Nkhani ikuti Antiokasi adzamva chiwembu chochokera kum’mawa ndi kumadera a kumpoto kuti mfumu ya Parthia akudza kudzathyola ufumu wake. Ichi, ndichimene chinapangitsa Antiokasi kusiya zonse anali kuchita ndi kupita kukalimbana ndi a Peresiya ndi Parthia, amene anaukira iye. Mfumu imeneyi,

inadzazidwa ndi ukari, kotero kuti anafuna kuononga kotheratu mtundu wa a Yuda wonse, koma anaphedwapaulendo umenewu.

Nkhani iyi, ikufotokonzedwa bwino ndi mkulu wina, wotchedwa Tacitus, amene akuyamikira Antiokasi chifukwa cha ntchito yomwe anayiyambayofuna kuchotsa zikhulupiriro za a Yuda ndi kulongamochikhalidwe cha a Greek, koma anaphedwamunkhondo ya Parthia, asanakwanitsechokhumbachakechi.

45. Ndipo adzamanga mahema a nyumba yachifumu yake pakati pa Nyanja yamchere ndi phiri lopatulika lofunika; koma adzafikira chimariziro chake wopanda wina wakumthandiza.

Ndiye nkhani ikuti, pamene Antiokasi anafuna kuononga a Yuda kotheratu, anamanga mahema a nyumba yachifumu pakati pa Nyanja yamchere ndi phiri lopatulika la Zioni. Kutsimikiza kuti anamanga nyumba yachifumu pa Emau, malo amene ali pafupi ndi Yerusalemu. Iye, anali kulingalira kuti pamene anamanga mahema ake aufumu, ngakhale iye atakhala kulibe anyamata ake ali ndi mphamvu yothira nkhondo pa a Yuda onse. Tsono kudzitama kwa Antiokasi kunaonekeranso pamene anamanga mahema ake paphiri lopatulika, limene ananena kuti ndi lake. Taonani wokondedwa

kuti, pamene uchimo ukula kuposa msinkhu, ndipo pamene chionongeko chifika.Uku, ndikukwaniritsa mau aja, akuti, “Koma adzathyoledwa popanda dzanja.”Kutsimikiza kuti pamene moyo ufikapokoma kwambiri, Mulungu amadzakuthyola ndi kuchotsa chonyadira, popanda wina wolepheretsa kugwa kwake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, pamene Mulungu abweransokudzathyola ndi kuononga onse wodzikweza ndi wozunza, sipadzakhalanso wina woleletsa kapena wofuna kuwathandiza ayi.Kutsimikiza kuti anthu onse amene amafunitsitsa kumalandira ulemu, panthawi yomweatchuka kwambiri ndiye pamene alowa m’mabvuto, sipapezeka wina wowakonda kapena kuwathandiza ngakhale kuwapempherera komwe.Kutsindika kuti ngati Mulungu sangawathandize, ndiyani amene angawathandize? Uku, ndiko kugwa kwawotsutsa Kristu kumene kulimkudzapatsiku limene wina aliyense sadzakwanitsakuleletsa.

Kwalerotilekeza pano. Koma timasanthulaDanieli 11:37-45, m’mene timaona za ufumu wodziika kuti ndiwo wanthawiyapang’ono.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!